

# KULAPA NDI CHIKHULULUKIRO



Lesson 11, June 6, 2026

“Koma tikavomereza  
machimo athu, Iye  
ndi wokhulupirika ndi  
wolungama ndipo  
adzatikhululukira  
machimo athu,  
nadzatiyeretsa ndi  
kutichotsera  
chosalungama  
chilichonse”

(1 Yohane 1:9, CCL)





Baibulo limanena kuti ‘onse anachimwa ndipo anaperewera pa ulemerero wa Mulungu’ (Aroma 3:23).




Limanenanso kuti sitingathe kupewa kapena kuchotsa tchimo lathu tokha (Yeremiya 13:23; 2:22).

Koma Mulungu ndi wokonzeka kutikhululukira machimo athu. Palibe tchimo lalikulu kapena loopsa kwambiri loti Mulungu sangafune kulikhululukira (Yesaya 1:18).

Pali chinthu chimodzi chokha chofunika: kulapa..





**Kulapa:**

-  Kuchedwetsa kulapa
-  Kulapa koon
-  Kuitanidwa ku kulapa



**Chikhululukiro:**

-  Chisomo cha chikhululukiro
-  Zovala za chikhululukiro



# KULAPA



# KUCHEDWETSA KULAPA

**"Ambuye anati, "Marita, Marita, ukudandaula ndi kuvutika ndi zinthu zambiri"  
(Luka 10:41 ccl)**


**Kunyumba kwa Lazaro, esu adalankhula za zinthu zofunika, zofunika kwambiri kuti munthu apulumuke. Koma Marita sanamvetsere. Analibe nthawi. Panali zinthu zambiri zoti achite! (Luka 10:40-41).**



**Izi zimachitikanso kwa ife. Tikachimwa, ndipo Mzimu Woyera atiyitana ku kulapa, Satana amatidzaza ndi ntchito zambiri, nkhwawa, kapena zosokoneza zina zilizonse zimene zimatilepheretsa kuganizira za mkhalidwe wathu wa uchimo ndi kufunafuna chikhululukiro.**



**Koma Mulungu satopa nafe. Iye amapitirizabe kutiyitanira kwa iye (Ezekiel 33:11). Amayerkezera machimo athu ndi zovala za sanza (Yeseya 64:6). Iye akutipatsa mwayi wosinthana: zovala zathu za sanza ndi zovala zake zoyera (Zekaliya 3:4), zovala zochapidwa m'mwazi wa Yesu (Chiv. 7:14).**



# KULAPA KOONA


**“Bwerani, tiyeni tibwerere kwa Yehova. Iye watikhadzula, koma adzatichiritsa. Iye wativulaza, koma adzamanga mabala athu.” (Hoseya 6:1 CCL)**

**Kodi kulapa ndi chiyani? Kodi pali kusiyana kotani pakati pa kulapa koono ndi kulapa kwachinyengo? (2 Akorinto 7:10)**

**Tchimo limabweretsa zotsatira zosafunika mwachangu, chisoni chimabwera. Timachita manyazi chifukwa chakuti zimene tinachita sizinayende bwino. Pakanakhala kuti zotsatira zoipa sizinakonekere, sitikanamva chisoni chifukwa cha zochita zathu. UKU SIKULAPA KOONA.**

**Pamene chisoni chibwera chifukwa cha tchimo lenilenilo limene tachita, ndipo timakhala ndi chikhumbo chozama chofuna kukhululukidwa (kaya pakhala zotsatira zoipa kapena ayi), ndiye kuti tikukumana ndi kulapa koono.**

**Tikachimwa, Mzimu Woyera amatidzudzula kwambiri ndi kutipatsa chisoni chozama chifukwa cha tchimo lathu. Tikayankha ndi kulapa koono, Mulungu amatichiritsa ndi kutikhululukira machimo athu (Hoseya 6:1)**



# KUITANIDWA KU KULAPA

**“Chifukwa chake, lapani, bwererani kwa Mulungu, kuti machimo anu afafanizidwe, kuti nthawi ya kutsitsimuka ibwere kuchokera kwa Ambuye.” (Machitidwe 3:19)**

Yohane M’batizi ndi Yesu anayamba utumiki wawo ndi uthenga womwewo: ‘Lapani’ (Mateyu 3:1-2; 4:17).

Nchifukwa chiyani kulapa kuli kofunika? Chifukwa popanda katero palibe chikhululukiro cha machimo (Machitidwe 2:38; 3:19). Kodi ndondomeko imeneyi imachitika bwanji?



**Chifukwa cha kukoma mtima kwake, Mulungu amatiyitanira ku kulapa (Aroma 2:4)**

**Timayankha kuitana Kwake**

**Mulungu amatikhululukira machimo athu chifukwa cha mwazi umene Yesu anakhetsa pa mtanda (Akolose 1:13-14)**

**Ndi chisoni chenicheni chifukwa cha zolakwa zomwe zachitika**

**Ndi chisankho choona mtima chosiya tchimo**

**Dziwani kuti kulapa ndi chikhululukiro ziyenera kutitsogolera ku kusintha nthawi zonse; kusintha kwa khalidwe komwe kumatitsogolera kuleka kuchimwa (Yohane 5:14).**





# CHIKHULULUKIRO



# CHISOMO CHA CHIKHULULUKIRO

“Chifukwa cha dzina lanu, Inu Yehova, khululukireni mphulupulu zanga,  
ngakhale kuti ndi zochuluka” (Masalimo 25:11) CCL



Palibe chimene chimakakamiza Mulungu kutikhululukira. Palibe chimene tingachite kuti tiyenere chikhululukiro chimenecho. Mulungu amatipatsa chikhululukiro mwa chisomo chake; chifukwa cha chikondi chake chopanda malire. Amakhululukira chifukwa ndi ‘wabwino, wokonzeka kukhululukira, ndi wochuluka mu chifundo’ (Masalimo 86:5; onaninso Eksodo 34:6-7).

Chikondi chake chinamtsogolera kudzipereka yekha pa mtanda, ndi kulipira ngongole ya tchimo imene sitingathe kulipira (Aefeso 2:4-5).



Tikabweretsa machimo athu pansu pa mtanda, Yesu amatimasula ku katundu wotilemetsa (Aheb. 12:1-2)



# CHISOMO CHA CHIKHULULUKIRO

“Chifukwa cha dzina lanu, Inu Yehova, khululukireni mphulupulu zanga,  
ngakhale kuti ndi zochuluka” (Masalimo 25:11 CCL)

Kodi pali ubale otani pakati pa tchimo ndi chisomo?

## UBALE PAKATI PA TCHIMO NDI CHISOMO

Aroma 5:8

“pamene tinali  
ochimwabe”

“Khristu  
anatifera”

Aroma 5:20

“pamene  
machimo  
anachuluka”

“chisomo  
chinachuluka  
koposa”

Aroma 5:21

“tchimo linkalamulira  
anthu ndi kubweretsa  
imfa pa iwo”

“chisomo chilamulire  
... kuwafikitsa ku  
moyo wosatha”

Aroma 6:23

“Pakuti mphotho  
yake ya uchimo  
ndi imfa”

“mphatso  
yaulere ya  
Mulungu ndiyo  
moyo wosatha”



# ZOVALA ZA CHIKHULULUKIRO

**"Anamufunsa kuti, 'Bwenzi walowa bwanji muno wopanda zovala zaukwati?' Munthuyo anakhala chete." (Mateyu 22:12)**

Mpingo wa Mulungu—ndipo potero chiwalo chilichonse cha mpingowo—chavala 'nsalu yabwino, yoyera ndi yonyezimira,' ndipo ali 'wopanda banga kapena khwinya kapena chinthu chilichonse chotere' (Chivumbulutso 19:8; Aefeso 5:27).

Nsalu yabwino imeneyi ndi chizindikiro cha 'ntchito zolungama za oyera mtima' (Chivumbulutso 19:8b). Koma chilungamo chimenechi si chawo; chinaperekedwa kwa iwo ndi Khristu (Chivumbulutso 7:14).



Pamene Adamu ndi Hava anachimwa, anaphimba maliseche awo ndi ntchito za manja awo. Koma ankadzionabe kuti anali amaliseche pamaso pa Mulungu (Genesisi 3:7-10). Chovala chimene Mulungu anawapatsa chinali chizindikiro cha 'chovala chaukwati' chimene Khristu amapereka: chilungamo chake changwiro chimene chimafafaniza machimo athu (Genesisi 3:21; Masalimo 51:7-10).

Palibe amene adzalowe Kumwamba popanda chovala chimenecho (Mateyu 22:1-14).



**“Iye amene akufuna kukhala mwana wa Mulungu ayenera kulandira choonadi chakuti kulapa ndi chikhululukiro zimapezeka kudzera mu nsembe yolipirira ya Khristu yokha. Pokhala ndi chitsimikiziro cha ichi, wochimwayo ayenera kuchitapo kanthu mogwirizana ndi ntchito yomwe adamchitira, ndipo ndi pemphero losaleka ayenera kupempha pampano wachifumu wa chisomo, kuti mphamvu ya Mulungu yakusinthazinthu ilowe m'moyo mwake. Khristu samakhululukira aliyense kupatula wolapa, koma amene amamukhululukira choyamba amam'patsa mtima wokulapa. Zokonzekera zonse zimapangidwa mwathunthu, ndipo chilungamo chamuyaya cha Khristu chimaikidwa pa moyo wa aliyense wokhulupirira. Chovala chamtengo wapatali, chosapasuka, cholukidwa m'makina akumwamba, chakonzedwa chifukwa cha wochimwa amene watembenuka mtima ndi kukhulupirira.”**